Kodi ndikatundu wanji yemwe ali wololedwa kutumiza pa ndondomeko ya m'bungwe la SADC?

Katundu yemwe ali wovomerezeka ndondomeko imeneyi ndi katundu amene akukwanilitsa ndondomeko ya (imene pachizungu amati *Rules of Origin)* kuthandauza kuti katundu yemwe ali wovomerezeka kuti wapangidwa kapena kulimidwa mdziko lomwe akuchokera.

Kodi pali china chofunika kudziwa pa ndondomeko ya malonda mbungwe la SADC?

Mbungwe la SADC muli maiko ambiri. Izi zikupangitsa munthu wa bizinesi kuti akhale ndi mwayi wa ukulu kugulitsa kapena kukagula katundu wogulitsa mdziko muno.

Ngati mugula katundu wanu kunja kapena kutumiza ku maiko ena pa ndondomeko ya m'bungwe la SADC, ndiye kuti mudzapindula kwambiri chifukwa choti mukatsatira zonse zofunikira ndiye kuti misonkho ina mudzalipira motsika kapena osalipira kumene.

Izi zidzapangitsa kuti mugule katundu kunja kapena kutumiza kunjako pa mtengo wotsika. Izi zidzapangitsa kuti mupindule kuposa anzanu ndikukulitsa bizinesi yanu.

Produced by Corporate Affairs Division-MRA

Malawi Revenue Authority
Msonkho House, Independence Drive
Private Bag 247
Blantyre

Tel: +265 - 1 822 588
Fax: +265 - 1 822 302
E-mail: mrahq@mra.mw
Web: www.mra.mw

Develop Malawi, Pay Taxes

ZA KUCHITA MALONDA M'DERA LA SADC

JULY 2017- JUNE 2018

SADC

NDI NDONDOMEKO YA MALONDA YOPINDULITSA



Kodi SADC ndi chiyani?

SADC ndi mau omwe akuthandauza kuti Southern Africa Development Community ndipo ndi mgwirizano wa malonda amaiko a kumwera. Bungweli linakhazikitsidwa mumzinda wa Windhoek mdziko la Namibia mchaka cha 1992.

Nanga mumgwirizano umenewu muli maiko angati?

Mumgwirizano wa SADC pakalipano muli maiko kapena mamembala okwanira khumi ndi mphambu zinai (14). Maikowa ndi monga Angola, Botswana, the Democratic Republic of Congo (DRC), Lesotho, Madagascar, Malawi, Mauritius, Mozambique, Namibia, South Africa, Swaziland, Tanzania, Zambia ndi Zimbabwe.

Kodi nanga Mmalawi wa bizinesi achite chiyani kuti apindule ndi mgwirizano umenewu?

Aliyense ndi wololedwa kuchita malonda mmaiko a SADC ndikupindura podzera mgwirizano umenewu. Mwa Chitsanzo, ngati munthu akufuna kugulitsa katundu kunja kwa dziko lino, katunduyo ayenera kukhala opangidwa kapena kulimidwa ku Malawi konkuno.

Iye ayenera kutenga chikalata chotchedwa Certificate of origin kuchokera ku ofesi ya Msonkho ku MRA monga ku Blantyre, Lilongwe kapena Mzuzu. Chikalata chimenechi chimagulitsidwa pa mtengo wa K50.00.

Munthu wa biziness ayenera kulembapo zofunikira zonse pa chikalatachi ndipo akatero, ayenera kuphatikiza makalata ena otumizira katundu kunja ndikupereka zonse ku MRA (Customs) kuti azisainile. Akatero iye atha kutumiza katundu wake kumaiko

akunja ndi kulipira misonkho yochepa kapena mwina osalipira kumene. Chimodzi-modzi ngati munthu ukufuna kubweretsa katundu wa malonda kubwera kuno kumudzi ayeneranso kutsatira ndondomeko ngati yomwe yatsatiridwa potumiza katundu kunja ngati dziko lomwe akuchokera katunduyo kubwera kuno ku Malawi lili nawo m'bungwe limeneli la SADC.